NYA_TTB_0894_20160901_**script**

Ezekieli : 16:15-18:32

Mutu : Mphotho yauchimo ndi imfa mu Yerusalemu

Ndikupatsani moni wa Kumwamba inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero ndi tsiku lina momwe talandira chisomo chokhala ndi moyo. Tere tiyeni Mulungu atitsogolere ndi mau apa Danieli 4:36, amene akuti, "Iye achita mwa chifuniro chake m'khamu la Kumwamba ndi mwa okhala pa dziko lapansi; ndipo palibe woletsa dzanja lake, kapena wakunena naye, muchitanji?"

Tsono mupologalamu yapita tinali kukambirana kuchokera pa Ezekieli 14:1-16:14, m'mene timaunika za ulosi wodzudzula chipembedzo chamafano ndi kuonetsa za chionongeko cha Yerusalemu. Ndipo lero pamene tipitiliza Ezekieli 16:15-18:32, tiona nkhani yakutsimikizakuti mphotho ya uchimo ndi imfa pa mzinda wa Yerusalemu.

Ezekieli 16

15. Koma unatama kukongola kwako, ndi kuchita zachigololo potama mbiri yako, ndi kutsanulirazigololo zako pa munthu ali yense wopitapo; unali wake.

Nkhani ili pano ikufotokonza za uchimo waukulu wa Israeli, maka-maka uchimo wopembedza mafano. Uwu, ndiwo uchimo wachigololo umene Yehova akunena kuti Israeli anachita.Ichi, ndichimene chinamunyasa kwambiri Mulungu chifukwa Israeli anachita chimenechi,posaona zokoma zomwe Mulungu anamuchitira m'mbuyomu.Tikunena kuti m'mbuyomo Yehova anachitira Israeli zinthu zambiri zazikulu koposa mtundu wina wonse, kotero kuti kunali koyenera kuti Israeli akhalebewoyamika Mulungu wake.

Ndiye m'chitidwe uwu, ndi umene ukufanana ndi kuphwanya pangano la ukwati ndi Mulungu. Kutanthauza kuti Israeli akufanizidwa ndi mkazi wadama, amene wasiya mwamuna wake ndi kukangamira mwamuna wachilendo. Chimene anachita Israeli ndi chakuti, anatsanulira chikondi chake ndi kutumikira milungu ina, yomwe ili adani a Mulungu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, tsono mwina inu mwafunsa kale kuti, kodi Israeli anachitiranji chimenechi?Yankho likuti, achinyamata athu ambiri aonongeka chifukwa cha mtima wodzikweza pakuona kukongola kwawo.Uwu, ndiwo mtima umene

unalowa mwa Israeli. Pachifukwa chimenechi inu ndi ine, tiyenera kumadzisanthula ndi kuona kuti ife, tiri monga momwe tiri chifukwa cha chisomo cha Mulungu.

53. Ndipo ndidzabwezaundende wawo, undendewa Sodomo ndi ana ake ndi undende wa Samariya ndi ana ake ndi undende wa andende ake, pakati pawo.
54. Kuti usenze manyazi ako, ndi kuti uchite manyazi chifukwa cha zonse unazichitapakuwatonthoza.
55. Ndipo abale ako Sodomo ndi ana ake adzabwereraumounakhalira kale; ndi iwe ndi ana ako mudzabwereraumomunakhalira kale.

Tsono ndi koyenera kunena kuti ndime izi, pamodzi ndi chapter 37, zakhala zikugwiritsidwa ntchito ndi anthu azipembedzo za mpatuko, pakuphunzitsa kuti anthu onse adzapulumuka. Anzanga, ganizo ililinadza chifukwa chokhazikika pa ndime imodzi yokha, osaona kumene nkhani ikuchoka ndi kumene ikupita. Taonani pa Ezekieli 37:12, Mulungu akunena kuti, “Chifukwa chake, nenera, nunene nawo, atero Ambuye Yehova taonani anthu anga, ndidzatsegulakumanda kwanu ndi kukweza inu

muturukem'manda mwanu ndipo ndidzakulowetsani m'dziko la Israyeli." Kutanthauza kuti mtundu wosankhidwawa Israeli udzabwezeretsedwanso kuchokera ku ukapolo wawo. Zomwe zikuimira moyo wachikristu, kuti ngati inu mudakhulupirira Yehova, kudzera mwa Ambuye Yesu Kristu, ndiye kuti ndinu amene munabwezeretsedwakuulemererowa Mulungu.

Tere, pano Mulungu akutsimikizirakuti adzasungamapangano ake ndi mtundu wa Israeli. Kutsimikiza kuti kupandukakwaIsraeli ndi kuchoka pamaso pake nthawi ndi nthawi, sikudzakhozakuphwanyitsa pangano la Mulungu ndi iwowa. Iyi, ndiyo nkhani yomwe Ambuye Yesu anatsindika pa Yohane 10:28, pamene anati, "Ndipo Ine, ndizipatsa moyo wosatha; ndipo sizidzaonongeka ku nthawi yonse, ndipo palibe munthu adzazikwatura m'dzanja langa." Kunena iwo amene anasankhidwamwachikhulupiriro chawo mwa Ambuye.

60. Koma ndidzakumbukila Ine pangano losathanawe.
61. Pamenepo udzakumbukila njira zako ndi kuchita manyazi, pakulandira abale ako akuru ndi ang'ono; ndipo

ndidzakupatsa awa akhale ana ako akazi, angakhale sali a pangano lako.

62. Pakuti ndidzakhazikitsa pangano langa ndi iwe, ndipo udzadziwa kuti Ine, ndine Yehova;

63. Kuti uzikumbukila ndi kuchita manyazi ndi kusatsegulanso pakamwa pako konse, chifukwa cha manyazi ako, pamene ndikufafanizira zonse unazita, ati Ambuye Yehova.

Tsono pamene Ezekieli akutseka chapter ichi, atatha kuwaonetsa uchimo wawo ndi kupereka chilango, tikuona kuti chifundo chikukumbukirika, komanso kuti chimasungidwakwa iwo amene adzabwera pambuyo pa mtundu wolonjezedwawo. Taonani pamene Mulungu analumbira mu mkwiyo wake, zinapangitsa kuti onse, amene anaturuka mwa Aigupto, asakalowa mu Kanani.Komaanakumbukira ana awo kuti ndiwo akalowa m'dziko lamalonjezano. Tere uku, ndiko kukwaniritsa kwa pangano lomwe analonjeza a Yuda pamene anatengedwa ukapolo ku Babulo. Tsono ngakhale a Yudawa anawabwezeretsa ku Yerusalemu, koma pangano ili, linakwanitsidwa m'nthawi ya Uthenga Wabwino kuti

padzakhala kulapa ndi chikhululukiro chimene chidzalalikidwa ku mitundu yapa dziko lonse, kuyambira m'Yerusalemu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, nkhani ili pano ikunena kuti, pamene Mulungu akumbukira pangano lake mwa ife, sakumbukiranso uchimo wathu pa ife ayi, koma amaikachikumbumtima mwa ife kuti tikhoze kuchita manyazi ndi kulapa machimowo.

Tsono pamene tiwerenga verse 60 mpaka 62, tipeza kuti Mulungu akunena kuti adzakhazikitsansopangano lake molimba ndithu, koposa kale. Ichi, ndicho chinthu cholimbikitsa kwambiri kuti lonjezano la chisomo cha Mulungu pa inu ndi ine, ndilo lokhazikika bwino kotero kuti ndilimenelimatikhazikaife nthawi yonse mupangano la Mulungu. Kutsimikiza kuti anthu onse amitundu ina, amene alandira lonjezano la chisomoli, nawonsoadzakhazikikamupangano la Mulungu lomweli. Kunena kuti pamene anthu amitundu inaadzaphunzitsidwaUthenga Wabwino, adzasungidwa nalowa m'chiyanjano ndi Mulungu wa Israeli, apa ndipo pamene adzatchulaYerusalemu kuti ndiye mayi. Iyi, ndinkhani imene Paulo pa Agalatiya 4:26, akuti, "Koma

Yerusalemu wa Kumwamba aliwaufulu, ndiwo amayi wathu." Kutanthauza kuti anthu amitundu inawa, adzatchulidwa kuti ndiwo alongo, osati chifukwa chapangano lina, kaya chifukwa chakukhalaantchito a Yuda, kapena chifukwa cha chipembedzo cha chi Yuda ayi, koma chifukwa chakutembenuka mtima m'chipembedzo cha chikristu. Momwemonso inu, mwina mukhoza kumaganizira za chipembedzo chanu, mtundu wanu ngakhalenso khungu lanu, koma mukhoza kuwerengedwamwana wa Mulungu chifukwa cha chikhulupiriro chanu mwa Ambuye Yesu Kristu, amene ndiye mwini chipembedzo chachikristu. Ndiye tikutsindika kuti, iwo amene amakumbukira machimo awo moona mtima, amachitanawo manyazi machimowo, kotero kuti samawiringula pamaso pa Mulungu. Kodi inu, mumachita manyazi ndi zolakwa zanu?Nkhani ikuti, pamene inu mukumva chisoni ndi kuchita manyazi ndi machimo anu, Mulungu kudzera mwa Ambuye Yesu Kristu, ndiye amapereka mtendere chifukwa chakuti mtanda wake ndiwo umene unatiyanjanitsakwa Mulungu. Ichi, ndicho chithunzi chomwe tikuchiona kuti pamene mwana wolowerera analandira mpsyopsyonowa atate wake, anakhala ndi chitsimikizo chonse kuti atate wake, anachotsa mkwiyo wawo pa iye. Tere, ndichifukwa

chake analimba mtima ndi kuwauza atate kuti anachimwira Kumwamba komanso iwo. Ndiye tikunenetsa kuti pamene manyazi akula chifukwa cha machimo athu mwakukhululukidwakwa machimo athu, mtendere ndi chitonthozo chathu mwa Mulungu chimachulukanso.

Ezekieli 17Mwambi wa ziombankhanga ziwiri

1. Ndipo anandidzera mau a Yehova, akuti,
2. Wobadwa ndi munthu iwe, iphamwambinunenefanizokwa nyumba ya Israeli.

Mneneri Ezekieli akuuzidwa kuphamwambi ndi kunena fanizo ku nyumba ya Israeli chifukwa anthuwa sanamumvere, kotero kuti Ezekieli anayenera kudza kwa anthuwa mwanjira ina.

3. Nuziti, atero Ambuye Yehova, chiombankhanga chachikuru ndi mapiko akuru, ndi maphiphiatali, odzalanthenga cha mathotho-mathotho, chinafika ku Lebano, nichitengansonga ya mkungudza,

4. Chinabudulansongayosomphoka ya nthambi zake zanthete, ndi kumuka nayo ku dziko la malonda, chinaiikam'mudziwa amalonda.
5. Chinatengakonso mbeu ya m'dziko, ndi kuibzalam'nthakayokoma, chinaiika panali madzi ambiri, chinaioka ngati mtengo wamsondodzi.

Tsono chiombankhanga chachikulu, ndicho chithunzi cha Babulo ndi mfumu Nebukadneza m'mau a Mulungu. Tere, tamvani Ezekieli 49:22, akuti, "Taonani, adzafikanadzauluka ngati chiombankhanga, adzatambasuliraBozira mapiko ake, ndipo tsiku lomwelo mtima wa anthu amphamvu a Edomu adzakhala ngati mtima wa mkazi alinkudwala." Koma Danieli 7:4, adaona ufumu wa Babulo ukuturukam'nyanja, umene udaoneka ngati mkango, wokhala ndi mapiko a chiombankhanga. Tere, ichi ndichitsimikizo chakuti chiombankhangachikuimira Nebukadneza, mfumu ya Babulo, amene wadza kudzadulansonga ya mtengo.Kunena Israeli, kuti ndiye mtengo, maka-maka nyumba ya Yuda. Kutanthauza kuti Nebukadneza ndiye amene adule ufumu wa Davide, monga muja anachitira ndi Zedekiya.

7. Panalinsochiombankhanga china chachikuru, ndi mapiko akuru ndi nthenga zambiri; ndipo taona, mpesa uwu unachipindira mizu yake, nuchilunjikitsira nthambi, kuti uphuke nthambi, nubale zipatso, nukhale mpesa wabwino.

Tsono chiombankhanga china ndi Aigupto, popeza ndiye amene anakula mphamvu m'nthawi imeneyo.Zedekiya ndiye amene anakhazikitsidwa pampando ndi mfumu Nebukadneza, kotero kuti analowa mupangano awiriwa. Koma taonani kuti Zedekiya sanasungepangano lake, kotero kuti anakopeka, nakhala paubwezi ndi Aigupto. Tere, iyi ndiyo nthambi ya Israeli yoweramira ku Aigupto. Kunena kuti mpesa wameram'nthaka ya Aigupto, kotero kuti mpesawuufuna kupeza mphamvu yake kuchokera kwa Aigupto. Koma taonani kuti izi, sizitheka chifukwa posachedwa Nebukadneza aononga Aigupto, ndikukhalamkwapa mwake.

Tiyeni tsono tione Uthenga kuchokera m'fanizo limeneli:

12. Uziti tsono kwa nyumba ya mpandukoyi, simudziwa kodi izi nchiyani? Uziti, taonani mfumu ya ku Babulo inadza ku Yerusalemu, nitenga mfumu yake ndi akalonga ake, nibwera nawo kuli iye ku Babulo;

13. Nitenga wa mbumba yachifumu, ndichita naye pangano, nimlumbiritsa, nichotsa amphamvu a m'dziko;
14. Kuti ufumuwu ukhale wopepuka, kuti usadzikweze, koma kuti pakusunga pangano lake ukhale.
15. Koma anapandukira ndi kutuma mithenga yake ku Aigupto, kuti ampatseakavalo ndi anthu ambiri. Adzapindula kodi? Anadzapulumuka wakuchita izi? Atyole pangano ndi kupulumuka kodi?

Nkhani mundime iyi, ikuti Israeli ndiye anaukira Yehova, ndipo pamene ali chikhalire pansi pa ulamuliro wa Nebukadneza, tikumva kuti anamuukiranso, natembenukira ku Aigupto. Kutsimikiza kuti Yuda sadasunge pangano lake ndi Nebukadneza.Tsono ichi ndichimene chikuchititsa chidwi kuti, Nebukadezamkunja, ndiye ameneanasunga pangano pamene Yuda, wodziwa Mulungu woona ndiye anaphwanya pangano.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ichi ndicho chithunzi cha mipingo yathu lero lino, kuti anthu amakangalikabe kutenga mabaibulo, koma mitima yawo ili kutari ndi Mulungu, kotero kuti simungakhulupirire zimene iwo amalankhula. Ndiye taonani kuti

pali anthu ena amene ndi akunja, koma amachita malonda awo mokhulupirika. Kodi inu muli m'gulu la anthu oukira Mulungu?

Ezekieli 18

Mu chapter 18, tiona kuti Mulungu akupereka chilango kwa munthu pa iye yekha.

1. Ndipo anandidzera mau a Yehova akuti,
2. Mutani inu ndi kunena mwambi uwu za dziko la Israeli, wakuti, Atate adadyamphesazosacha, ndi mano a ana ayayamira.

Mundime iyi, muli mwambi wakuti Atate adadyamphesazosacha, ndi mano a ana, ayayamira, umene umafanana ndi mwambi wakuti, nkhuyuzodya mwana zinapotamkulu. Miyambi imeneyi ikufanana paganizo lakuti, tchimo lochita munthu wina, limakhudza wina. Tere munkhani iyi, Yuda amene ndi ufumu wa kum'mwera akunena kuti akulangidwa chifukwa cha uchimo wa mfumu Manase. Kutanthauza kuti a Yudawa, akudziyeretsa kuti sanachimwe kotero kuti anali angwiro ndipo anali kulangidwa chifukwa cha tchimo la makolo awo.Komanso ponena mwambi

umenewu, akutanthauza kuti Mulungu sanachite chilungamo kotero kuti anawachitirankhanzapowatengera ku Babulo ku ukapolo.Kutsimikiza kuti ngakhale anthuwa anali kulandira chilango, koma sadalape.Ndiye tikunena kuti ndi munthu watsoka amene akangana ndi Mlengi wake.Kodi inu mulibe mtima uwu, wodziyeretsa?

3. Pali Ine, ati Ambuye Yehova, simudzaonanso chifukwa cha kunena mwambiwum'Israeli.
4. Taonani, miyoyo yonse ndi yanga, monga moyo wa atate momwemonso moyo wa mwana, ndiyo yanga; moyo wochimwawo ndiwo udzafa.

Tsono pano Mulungu akunena kuti Yuda sayenera kugwiritsa ntchito mwambi umenewu, chifukwa moyo uliwonse uli m'dzanja lake. Komanso Yuda sayenera kudziyeretsa chifukwa pamene akulimbikira kudziyeretsa ndiye kuti akuchimwa, kotero kuti munthu aliyense adzalangidwa chifukwa chosafunakutsutsika.

Nkhani ikunena kuti Mulungu salanga ana chifukwa cha uchimo wa atate awo, pokha-pokha anawoakuyendamutchimo la atate awo. Iyi, ndinkhaniimene Ambuye Yesu pa Mateyu 23:32, adati, "Dzazani

inu muyeso wa makolo anu." Kutsimikiza kuti a Yuda awa samayenera kudandaula popeza iwoanachimwanso monga makolo awo.Taonani pamene tiwerenga Deuterenomo 24:16, tipeza mau otsimikiza akuti, "Atate asaphedwere ana, ndi ana asaphedwere atate; munthu yense aphedweretchimo lake lake."Ichi, ndichifukwa chake akunenetsa kuti, "moyo wochimwawo ndiwo udzafa."

Tsono ma verse a 5-9, ndiwo amene akutsimikiza kuti munthu akakhala wolungama, nachita chiweruzo ndi chilungamo, wosadyapamapiripo, wosakweza maso ake kumafano, adzapulumuka. Kunena kuti ndikotheka mwana kubadwira m'banja loipa, koma iye akasankhakuleka kulambira mafano, kapena akasiya tchimo la pabanja lake, adzapulumuka ndithu. Momwemonso munthu wolungama, akhoza kubala mwana woipa.Kutanthauza kuti pamene mwana akula, akhoza kusankhakusamvera Mulungu, kotero kuti adzalangidwa chifukwa cha mphulupulu zake. Kunena kuti Mulungu apa, sangalange atate wake, koma mwanayo.

14. Taona tsono, yemweyo akabala mwana uyu, naonazochimwa zonse adazichita atate wake, naopawosachitazoterezo;

15. Wosadyapamapiri, kapena kukweza maso ake ku mafano a nyumba ya Israeli, wosaipsa mkazi wa mnansi wake,
16. Kapena kusautsa wina aliyense, wosatengachigwiriro, wosatengazofunkha; koma anapatsawanjala chakudya chake, nabvekawamariseche ndi chobvala,
17. Naletsa dzanja lake pa wozunzika, wosalandira phindu kapena choonjezerapo, wochita maweruzo anga, nayendam'malemba anga; uyu sadzafera mphulupulu ya atate wake, adzakhala ndi moyo ndithu.

Mau awa akunena kuti ndizotheka kuti mwana akhoza kusiya njira ya atate wake, amene ali woipa. Mwachitsanzo Ahazi anali mfumu yoipa, koma Hezekiya anali mwana wabwino, amene anatsogolerachitsitsimutso mu Yuda.Koma Yosiya analinso mfumu yabwino pamene anali ndi atate woipa kwambiri.

31. Tayani ndi kudzichotsera zolakwa zanu zonse zimene munalakwa nazo, ndi kudzifunira mtima watsopano ndi Mzimu watsopano, pakuti mudzaferanji inu, nyumba ya Israeli?

32. Pakuti sindikondwera nayo imfa ya wakufayo, ati Ambuye Yehova; chifukwa chake bwererani, nimukhale ndi moyo.

Wokondedwa anzanga apaulendo, tiyeni titsirize ndi mau akuti, munthu aliyense adzaweruzidwa monga mwa tchimo lake. Koma taonani Mulungu akunenetsa kuti sakondwera ndi imfa ya munthu wakufa, kutsimikiza kuti munthu wochimwa ndi wakufa kale. Kodi inu munadzipereka kale kwa Ambuye Yesu amene achotsa tchimo la dziko lapansi?

Kwalerotilekeza pano. Timakambirana kuchokera pa Ezekieli 16:15-18:32, m'mene timaona nkhani yakutsimikiza za mphotho ya uchimo kuti ndi imfa pa mzinda wa Yerusalemu.

Ambuye akudalitseni inu lero. Amen!